RAPID

M F U N D O

Kugwirizana Komwe Kulipo Pakati pa Chiwerengero cha Anthu ndi Chitukuko m'Malawi

Kugwiritsa Ntchito Njira Yophunzitsira Anthu za Chiwerengero cha Anthu ndi Chitukuko Pokonzekera Tsogolo Lathu

December 2017

The Republic of Malawi

University of Malawi

Chiwerengero cha dziko la Malawi chikukwera kwambiri—chifukwa chakuti malinga ndi mbiri ya dziko lino anthu akhala akuberekana kwambiri komanso chifukwa chakuti chiwerengero cha anthu omwalira chakhala chikuchepa. Malinga ndi momwe chikukwelera chiwerengerochi kudzakhala kovuta kuti boma lidzakwanitse kusamalira anthu ake pa ntchito monga zaumoyo, maphunziro, chuma ndi zamalimidwe. Padzakhalanso mavuto ena pa chitukuko cha m'matawuni ndi ntchito zomangamanga kuphatikizapo ntchito yopereka madzi okwanira aukhondo ndi magetsi okwanira. Kukonza ndondomeko ndi ntchito zothandiza kuti Amalawi azitha kupeza mwakufuna kwawo chithandizo cha njira za kulera ndi kukwaniritsa zofuna zawo za uchembere zomwe zidzathandize kuchepetsa muyezo wa kaberekedwe komanso kuti chiwerengero chizikwera pang'onopang'ono.

Nthambi yowona za Chiwerengero cha Anthu mu Unduna wa Zachuma, Mapulani a Zachuma ndi Chitukuko pamodzi ndi Nthambi Yowona za Chiwerengero cha Anthu ku Chancellor College, ku Yunivesite ya Malawi—ndi thandizo lochokera ku Health Policy Plus Project yomwe imalandira thandizo lake kuchokera ku boma la Amerika—anagwiritsa ntchito Njira Yophunzitsira Anthu za Chiwerengero ndi Chitukuko yomwe pa Chingelezi imatchedwa Resources for the Awareness of Population Impacts on Development (RAPID) pofuna kuwunikira zotsatira zomwe zingadze kamba ka kukwera kwa chiwerengero pa ntchito zosamalira anthu ndi zachuma m'magawo osiyanasiyana a chitukuko. Zotsatirazi zikusonyeza momwe dzikoli lingadzakhudzidwire ndi kutsika kwa muyezo wa kaberekedwe kuchoka pa ana 4.4 pa mayi mmodzi mu 2015 kufika pa 2.3 mu 2050, kutsimikiza za kufunika kochitapo kanthu pofuna kuonetsetsa kufunika kokhazikitsa ntchito komanso ndondomeko zamphamvu zothandiza kuti chiwerengero chizikwera pang'onopang'ono komanso kuti ntchito zosamalira anthu ndi zachuma zipite patsogolo.

Muyezo wa Kaberekedwe

Muyezo wa kaberekedwe m'Malawi—kapena kuti mlingo wa ana amene mayi amabereka pamoyo wake wonse—watsika kwambiri m'zaka zapitazi. Komabe amayi ndi abambo akunena kuti amalakalaka atamakhala ndi chiwerengero chochepa m'banja chosapyora muyezo wa kaberekedwewu; mabanja akumakhala ndi ana oposa amene akuwafuna. Kupeza mwayi wa njira zakulera kungathandize kuthetsa vutoli.

Zotsatira za Kukwera Pang'onopang'ono kwa Chiwerengero

Ngati muyezo wa kaberekedwe utatsika, ndiye kuti boma lidzakhala ndi mwayi wopulumutsa chuma china chomwe lingagwiritse ntchito pa chitukuko, ndikuti lizitha kuchita zinthu mogwirizana ndi kukwera kwa chiwerengero m'magawo osiyanasiyana zomwe pamapeto pake zidzathandize kuti dzikoli likhale lotukuka.

Kakweredwe ka Chiwerengero Mtsogolo: Poyerekezera ndi Muyeso wa Kaberekedwe



Ngati muyeso wa kaberekedwe m'Malawi **ungatsike kuchoka pa ana 4.4 pa mayi mmodzi kufika pa 2.3:**

Chiwerengero chikuyembekezeka kudzafika **34.3 miliyoni m'chaka cha 2050,** chomwe ndi chotsikirako poyerekeza ndi **42.8 miliyoni** ngati kakweredwe ka chiwerengero kasasinthe

Chiwerengero cha zipatala zofunika kumangidwa podzafika chaka cha 2050

chidzakhala 371

Mulingo wa aphunzitsi amene angadzafunike m'chaka cha 2050 **udzachepa ndi 96,000**

Kachulukidwe ka chuma cha dziko pa munthu aliyense kakuyembekezeka

kudzakwera ndi 25 pelesenti

m'chaka cha 2050

Chimanga chimene chidzapulumutsidwe kuchokera 2015 kudzafika 2050 chidzakhala **matani 14 miliyoni**

M'chaka cha 2050 **chiwerengero cha anthu okhala m'matawuni**

chidzatsika ndi 2.6 miliyoni

M'zaka 35 zikudzazi madzi am'mipopi amene adzapulumutsidwe

adzakhala 407 miliyoni m^3

51 pelesenti ya chiwerengero cha anthu ikuyembekezeka kudzakhala ndi magetsi m'chaka cha 2050 poyerekeza ndi 41 pelesenti ngati kakweredwe ka chiwerengero sikasintha

Zomwe Tingachite

Kutukula ntchito za kulera kumathandiza kukhala ndi zotsatira zaphindu m'magawo onse a chitukuko.

Kutukula ntchito zakulera kudzathandiza aMalawi kukwaniritsa zolinga zawo pa nkhani zauchembere komanso kuti chiwerengero chizikwera pang'onopang'ono. Cholinga cha dziko la Malawi pa za Ntchito za Kulera ndi chakuti podzafika chaka cha 2020 aliyense adzakhale ndi mwayi wopeza njira zakulera mwakufuna kwake ndipo kuti osachepera 60 pelesenti ya amayi onse adzakhale akugwiritsa ntchito njira zakulera zamakono. Kukwaniritsa cholinga chimenechi kudzafunika kukhala ndi chuma chokwanira komanso padzafunika kuonetsetsa kuti ntchito zonse zosamalira anthu zimene zikuchitika zikugwirizana ndi zolinga za ntchito zokhudza chiwerengero cha anthu ndi chitukuko. Magawo onse a ntchito zachitukuko angathe kupindula ndi kutsika kwa kakweredwe ka chiwerengero, ndipo ali ndi udindo wolimbikitsa kuonjezera chuma chogwirira ntchito za kulera.

Magawo Osiyanasiyana Angathandize Bwanji Polimbana ndi Kukwera kwa Chiwerengero.

Pofuna kuthana ndi zotsatira za kukwera kwa chiwerengero mopitiliza muyezo, magulu osiyanasiyana amene akukhudzidwa ndi nkhaniyi angathe kuphatikizapo ntchito izi mu ndondomeko za ntchito zawo:

- Kulimbikitsa kupeza chuma choyendetsera ntchito zakulera, kufalitsa mauthenga, chithandizo ndi zipangizo za kulera
- Kukonza ntchito zothandiza kuti atsikana asamasiyire sukulu panjira
- Kulimbikitsa ntchito zachi chisamaliro cha anthu
- Kutukula ntchito zaumoyo ndi umoyo wa ana
- Kupereka mwayi wa ntchito kwa achinyamata
- Kutukula njira zothandiza kuwonjezera zokolola ndi njira zosiyanasiyana zopezera chuma
- Kukopa anthu pa ntchito zotukula zomangamanga m'matawuni, madzi aukhondo ndi magetsi

Kutukula ntchito zakulera kungathandize kupititsa patsogolo miyoyo ya nzika ndikuti dziko lithe kupindula ndi chitukuko cha ntchito za maphunziro, mwayi wa zachuma, ntchito zaumoyo ndi zofunikira zina za tsiku ndi tsiku monga chakudya, madzi aukhondo, ndi magetsi. Phindu limeneli lidzathandiza kuti dziko litukuke mokhazikika pa ntchito zosamalira anthu ndi zachuma ndikusintha dziko la Malawi kuti chitukuko chake chikwere kupita patsogolo.

Ndondomeko

Ndondomeko za dziko la Malawi—Masomphenya a Dziko la Malawi Pofika 2020 (Vision 2020), Ndondomeko ya za Chiwerengero cha Anthu komanso Ndondomeko Yachitatu ya Kukwera Kwa Chuma ndi Chitukuko—ndi zimene zikutsogolera pa masomphenya a chitukuko cha dziko lino kuphatikizapo pa chitukuko cha ntchito zosamalira anthu ndi chuma, chitukuko cha zaumoyo ndi kupereka mwayi wofanana kwa anthu onse. Kukwaniritsa zolinga za mu ndondomeko zimenezi kudzadalira mmene chiwerengero cha anthu adziko lino chidzakhalire m'tsogolo muno.

Mfundo zimene zalembedwa muno zachokera m'kabuku ka Dziko La Malawi kotchedwa 2017 *RAPID: Estimating the Impact of Population Growth on Development in Malawi.* Uthenga wowonjezera wa Njira Yophunzitsira Anthu Za Chiwerengero cha Anthu ndi Chitukuko m` Malawi mutha kuupeza pa http://populationmalawi.org.

Kuti mumve zambiri, funsani kwa:
Unduna wa Zachuma, Kukonza Mapulani a Zachuma ndi Chitukuko
Nthambi Yowona za Chiwerengero cha Anthu
P.O. Box 30136
Lilongwe 3, Malawi